# CHUMA CHOBISIKA M'BAIBULO

*Chomwe Akhrisitu*

*Sanachitulukirebe Mpaka Lero*

Lolembedwa ndi MI Anwar H. Bismilla

Latanthauzidwa m'Chichewa ndi

Peter Mota

ISLAMIC INFORMATION BUREAU

## ZA MKATIMU

## CHUMA CHOBISIKA M'BAIBULO


| **Mutu** | Tsamba |
|---|---|
| Zamkatimu | 3 |
| Mawu oyamba | 5 |
| MUTU 1: Mulungu m'Baibulo | 6 |
| MUTU 2: Kugwetsa nkhope pansi popemphera m'Baibulo | 10 |
| MUTU 3: Kupereka chaulere kwa anthu osowa, lamulo la m'Baibulo | 13 |
| MUTU 4: Kusala m'Baibulo | 15 |
| MUTU 5: Kuyeretsa ziwalo (mapemphero asanachitike) m'Baibulo. | 17 |
| MUTU 7: M'dulidwe m'Baibulo | 19 |
| MUTU 8: Nkhumba, nyama yodetsedwa m'Baibulo | 22 |
| MUTU 9: Mowa, chakumwa choletsedwa m'Baibulo | 29 |
| MUTU 10: Kuvala mpango m'mutu kwa azimayi podzilemekeza m'Baibulo | 31 |
| MUTU 11: Kulonjerana pofunirana mtendere m'Baibulo | 32 |
| MUTU 12: Katapira, mchitidwe oletsedwa m'Baibulo | 33 |
| CHISILAMU! | 35 |
| Mafunso ndi mayankho okhudza Chisilamu | 39 |
| Mawu omaliza | 45 |


***

# Mawu oyamba

Pafupifupi anthu onse amakhulupilira kuti kunali munthu wotchedwa Yesu (MUPI), koma iwo amasiyana momwe amamvera ndi kutsatira uthenga womwe iye ankaphunzitsa. Kuchuluka kwa mipingo ya Chikhrisitu ndi mitundu ya Baibulo masiku ano ndi umboni wokwanira wosonyeza kuti anthu amawumvetsa ndi kutsatira uthenga wa Yesu (MUPI) mosiyana. Funso nkumati: Kodi uthenga weniweni wachoonadi wa Yesu (MUPI) uli kuti?

Nanga ndianthu ati omwe amatsatira uthenga wachoonadiwu lero lino? Cholinga cha bukhuli ndi kuwaunikira anthu, omwe amafuna kudziwa zoona zokhazokha, pa zauthenga weniweni womwe Yesu (MUPI) ankaphunzitsa. Bukhuli likukamba za machitidwe ena omwe analetsedwa kapena kuvomerezedwa m'Baibulo. Pali chikhulupiliro chakuti anthu akawerenga bukhuli adzipezera okha gulu lenileni la anthu lomwe limatsatira chiphunzitso cha Yesu (MUPI). Umboni wochokera m'Baibulo ugwiritsidwa ntchito pofuna kuwaunikira awerengi athu chipembedzo chenicheni cha Yesu (MUPI) lero lino. Anthuwa ayenera kudziwa otsatira enieni a chiphunzitso cha Baibulo.

Akhrisitu lero lino samalabadira machitidwe a Yesu (MUPI) omwe ali m'Baibulo ngakhale machitidwewa ndi omwe ayenera kutenga gawo lalikulu pa chikhulupiliro chawo cha Chikhrisitu.

***

# MUTU 1

## Mulungu m'Baibulo

## Mulungu ndi Mmodzi

M'baibulo, dzina loti Mulungu limayimira Mlengi mmodzi yekha yemwe analenga zinthu zonse. Mulungu mmodzi yekhayu ndi yenwe ayenera kupembedzedwa.

Chipangano Chatsopano chikunena kuti:

*Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha yekha udzamlambira*." [Mateyu 4:10]

"*Yesu anayankhula kuti: …mvera Israyeli, Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi*. [Mariko 12:29]

Chipangano Chakale chikunena kuti:

"…*Ine ndili woyamba ndi womaliza, ndi popanda Ine palibenso Mulungu*" [Yesaya 44:6]

"*Ndipo palibenso Mulungu wina popunda Ine; Mulungu wolungama, ndi Mpulumutsi; palibenso wina popanda Ine. Yang'anani kwa Ine, mupulunmutsidwa... mabondo onse adzandigwadira ine*..." [Yesaya 45:21-23]

**Ndemanga**

Ndime za m'Baibulozi zikufotokoza momveka bwino za chithunzithunzi choona chenicheni cha Mulungu. Ichi ndichithunzithunzi chomwe atumiki a Mulungu onse monga Yesu ndi Mose (MUPI) anali nacho, ndipo atumiki onsewa ankawaitanira anthu ku chiphunzitso chimenechi. Ngakhale izi zili chonchi, chithunzithunzi cha Mulungu chomveka bwinochi sichikupanga gawo la chikhulupiliro cha Akhrisitu lero lino. Chikhulupiliro

chawo mwa Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera chikutsutsana kwambiri ndi chiphunzitso chomveka bwino choti Mulungu ndi **mmodzi yekha**.

Ndime za m'baibulo zomwe zasanthulidwazi zatiwunikira kuti Mulungu ndi mmodzi. Choncho, sikoyenera kutchula chinthu china chomwe chili kumwamba kapena padziko lapansi kuti Mulungu chifukwa Mulungu ndi **mmodzi yekha**.

## 'Utatu wa Mulungu' m'Baibulo

Pali ndime imodzi yokha ya m'Baibulo yomwe imayikira umboni kuti pali Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera. Koma ndime imeneyi simapezeka m'ma Baibulo a New International Version (NIV) komanso m'ma Baibulo a Revised Standard Version (RSV) chifukwa ndimeyi inachotsedwa. Pa zakuchotsedwa kwa ndimeyi, ma Baibulowa amati ndimeyi inachotsedwa chifukwa choti sinkapezeka m'ma Baibulo omwe ankalembedwa kalekale m'zaka za m'ma 1600. Ndime yomwe inachotsedwayi ili motere:

"*Pakuti pali atatu akuchita umboni, Mzimu, ndi Madzi, ndi Mwazi; ndipo iwo atatu ali mmodzi*." [1 Yohane (Buku Loyamba) 5:8]

## Utatu wa Mulungu?

## Mafunso ambiri; Mayankho ochepa

- Ngati Mulungu ali mmodzi wa 'Utatu', ndi chifukwa chiyani lye sanakambe za izi m'Chipangano Chakale?
- Kodi Yesu (MUPI) ananenapo zoti Iye ndi mmodzi wa 'Utatu wa Mulungu'? Nanga Mzimu Woyera' nawonso unakambapo za izi?
- Ngati Utatu wa Mulungu' ali maziko a chikhulupiliro cha chipembedzo, ndi chifukwa chiyani m'Baibulo palibe malo ena

pomwe pali mawu oti: Utatu wa Mulungu?

- Ngatidi 'Utatu wa Mulungu' ndi chikhulupiliro chopambana kwambiri ngati momwe amachitchukitsira, ndichifukwa chiyani chikhulupilirochi sichimatchuka Yesu (MUPI) asanabadwe?
- Ngati Yesu (MUPI) anafera machimo a anthu, ndindani yemwe anawafera machimo anthu omwe anamwalira iye 'asanawafere anthu machimo'?

## Mwana wa Mulungu?

Mawu oti 'Mwana wa Mulungu' m'Baibulo samatanthauza mwana weniweni woziberekera yekha Mulungu. Ngati Yesu (MUPI) alidi mwana weniweni wa Mulungu, ngati momwe Baibulo likunenera, ndiye kuti Adamu, Davide, Efraimu (MUPI) ndi ena otero ayeneranso kumatchedwa ana enieni a Mulungu chifukwa malingana ndi Baibulo nawonso ndi ana a Mulungu.

"..*ndipo Efraimu ali <u>mwana wanga woyamba</u>*" [Yeremiya 31:9]

"..*mwana wa Enosi, mwana wa Seti, mwana wa Adamu Imwana wa Mulungu*" [Luka 3:38]

"*Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu.*" [Aroma 8:14]

".*Yehova ananena ndi ine (Davide), Iwe ndiwe mwana wanga; <u>Ine Mulungu) lero ndakubala</u>.*" [Masalimo 2:7]

### Ndemanga

Zikuonetsa kuti mawu oti 'mwana wa Mulungu' sanatanthauziridwe moyenerera kuchokera ku chiyankhulo cha Chigiriki. N'kutheka kuti otanthauzira Baibuloli ku ziyankhulo zina ankafuna kutanthauza kuti 'kapolo wokondedwa wa Mulungu', osati 'mwana woziberekera yekha Mulungu' ngati momwe anthu amaganizira lero lino. Anthu akamakamba za 'mwana wa Mulungu'

n'kumatanthauza kuti ndi mwana <u>weniweni</u> woziberekera yekha Mulungu, ndiye kuti Davide (MUPI) nayenso ayenera kumatchedwa mwana weniweni wa Mulungu. Iyenso ayenera kumatchuka pakati pa anthu onse kuti ndi mwana Mulungu."

M'Baibulo, anthu ambiri kuonjezerapo Yohane akunenapo za 'ana a Mulungu: (19) "*Tidziwa kuti tili ife <u>(ndi ana) ochokera mwa Mulungu</u>.... (20) Ndipo tidziwa kuti <u>Mwana wa Mulungu</u> wafika, natipaisa ife chidziwitso kuti tizindikire...*" [1 Yohane 5:19-20]

M'Baibulo, Yesu (MUPI) akamamutchula Mulungu kuti Atate' akunena mokuluwika. Iye akugwiritsira ntchito liwuli ndi cholinga chopereka ulemu kwa Mulungu. Potero, Iye amakhalanso akusonyeza kuti iye ndi wokondeka wa Mulungu. Ichi ndi chifukwa chakenso pemphero lija la ana kwa Mulungu limayamba motere: "*Atate athu muli m'mwamba...*"

### Ndemanga yomaliza pa za umodzi wa Mulungu

M'Baibulo, palibe malo ngakhale amodzi omwe Yesu ananena kuti: "Ine ndi Mulungu" kapena "Ndilambireni". Kukanakhala kuti ichi chinali chiphunzitso chofunikiradi kwambiri mu Chikhrisitu, bukhu la Baibulo likanakamba za izi motsindika ndi momveka bwino.

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi chikhulupiliro chomveka bwino chakuti Mulungu ndi mmodzi chili kuti lero lino?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena samatsatira chikhulupilirochi?
- Nanga lero lino, ndianthu ati omwe amakhulupilirabe mu umodzi wa Mulungu?

***

## MUTU 2

## Kugwetsa nkhope pansi popemphera m'Baibulo

Baibulo limakamba zoti Yesu (MUPI) amapemphera pogwetsa nkhope yake pansi, ngati momwe Mose, Abrahamu, Davide (MUPI) komanso atumiki ena a Mulungu amachitira akamamupembedza Mulungu. Nawu umboni wochokera m'Baibulo:

1. **Yesu** (MUPI) anagwetsa nkhope yake pansi pochita mapemphero.

"*Ndipo anamuka patsogolo pang'ono nagwa nkhope yache pansi, napemphera, nati, 'Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire Ine; koma si monga ndifuna ine koma Inu.*" [Mateyu 26:39]

2. **Abramu** (MUPI) anagwetsa nkhope yake pansi pochita mapemphero. "*Ndipo Abramu anagwa nkhope pansi*... [Genesis 17:3]

3. **Mose** ndi Aaroni (MUPI) anagwetsa nkhope zawo nansi pochita mapemphero.

"*Ndipo Mose ndi Aroni anachoka pamaso pa msonkhano kumka ku khomo la chihema chokomanako, nagwa nkhope zawo pansi*..." [Numeri 20:6]

4. **Eliya** (MUPI) anagwetsa nkhope yake pansi pochita mapemphero.

"…*koma Eliya anakwera pamwamba pa Kurimeli; nagwadira pansi, naika nkhope yache pakati pa maondo ache.*" [1 Mafumu 18:42]

5. **Yoswa** (MUPI) anagwetsa nkhope yake pochita mapemphero.

"*Pamenepo Yoswa anagwa nkhope yache pansi, napembedza, nati*..." [Yoswa 5:19-20]

**Ndemanga:**

Mawu woti ‘napembedza’ mu ndime ili mumtundayi akuonetsa kuti Yoswa (MUPI) anagwa pansi osati ndi chifukwa china ayi, koma chomupembedza Mulungu mmodzi yekha basi.

6. **Davide** (MUPI) anagwetsa nkhope yake pansi popemphera. “…*Davide anauka chakumwera, nagwa nkhope yache pansi, nawerama katatu*...” [1 Samueli 20:41]

Ndime zina za m’ Baibulo zomwe zikuchitira umboni pa nkhaniyi ndi izi: “*Pamene Mose anamva ichi anagwa nkhope yache pansi*..” [Numeri 16:4]

“*Ndipo (Mose ndi Aroni) anagwa nkhope zao pansi, nati, Mulungu*...” [Numeri 16:22]

“*Ndipo Yoswa anang’amba zobvala zake, nagwa nkhope yake pansi, kulikasa la Yehova*...” [Yoswa 7:6]

“*Ndadzilumbira ndekha, mau achokera m’kamwa mwanga m’chilungamo, ndipo sadzabwera, kuti maondo onse Ndemanga Popemphera, Atumiki ndi aneneri onse adzandigwadira ine*...” [Yesaya 45:23]

<u>Ndemanga</u>

Popemphera, Atumiki ndi aneneri onse a Mulungu amagwada pansi nayika nkhope zawo pakati pa maondo awo, ngati momwe chikuonekera chithunzi chili m’musimu:



<u>Ndemanga</u>

Popemphera, Akhrisitu ambiri masiku ano amagwada, kuomba m’manja ndi kuchita zinthu zina zosiyaniranatu ndi zomwe Yesu

(MUPI) ankachita. Popemphera, Yesu (MUPI) ankachita zomwe atumiki onse a Mulungu ankachita. Iye ankagwetsa nkhope yake pansi.

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kugwetsa nkhope pansi popemphera unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino antha ena satsatira mtchitidwewu?
- Nanga lero lino, ndianthu ati omwe amalemekezabe ndi kutsatira mchitidwewu?

***

## MUTU 3

## Kupereka chaulere kwa osowa, lamulo la m'Baibulo

Kupereka chaulere kwa anthu osowa ndi lamulo la m'Baibulo. Choperekachi sichiyenera kukhala msonkho kapena mtuka wapachaka woperekа ku mpingo ayi, koma chiyenera kukhala chopereka chaulere chopita kwa anthu okhawo omwe ali aumphawi ndi osowa.

1. **Mose** (MUPI) alamulidwa kupereka chaulere kwa osowa

"*..chifukwa chake ndikuuzani ndikuti, dzanja lanu mulitansire ndithu m'bale wanu, ndi ozunzika anu ndi aumphawi anu, a m'dziko mwanu.*" [Deuteronomo 15:11]

"*Muzipereka ndithu limodzi la mbeu zanu, zofuma kumunda, chaka ndi chaka...*" [Deuteronomo 14:22]

Ndemanga

"Mtuka wapachaka ku mpingo' ndi gawo la chikhumi la zokolola zonse lomwe linakhazikitsidwa kuti liperekedwe kwa anthu osauka chaka ndi chaka." [Oxford Dictionary]

2. **Yesu** apempha anthu kupereka chaulere kwa osowa

"*Koma iwe popatsa mphatso zachifundo, dzanja lako lamanzere lisadziwe chimene lichita dzanja lako lamanja; kotero kuti mphatso zako zachifundo zikhale zam'tseri; ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.*" [Mateyu 6:3-4]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kupereka chaulere kwa anthu osowa unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena satsatira mtchitidwewu?

Nanga lero lino, ndianthu ati omwe amalemekezabe ndi kutsatira mchitidwewu?

***

# MUTU 4

## Kusala m'Baibulo

Tikasanthula Chipangano Chatsopano m'Baibulo, tipeza kuti Yesu (MUPI) ankasala. Atumiki onse a Mulungu omwe analipo Yesu (MUPI) asanabwere ankasalanso.

"*Ndipo pamene iye (Yesu) analibe kudya masiku makumi anayi usana ndi usiku, pambuyo pake anamva njala.*" [Mateyu 4:2]

"*Koma mzimu wa mtundu umenewu, pokhapokha mutayamba mwapemphera ndi kusala zakudya mpamene mungautulutse.*" [Mateyu (Buku Loyera) 17:21]

"*Ndipo anaunjikana ku Mizipa natunga madzi, nawatsanula pamaso pa Yehova, nasala chakudya tsiku lija...*" [1 Samueli 7:6]

<u>Nazi ndime zina za m'Baibulo zomwe zikuchitira umboni pa za kusala</u>

"*Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala chakudya... Pamenepo, m'mene adasala chakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke.*" [Machitidwe 13:2-3]

"*Ndipo anakhala pomwepo ndi Yehova masiku makumi anai, usana ndi usiku; sanadya mkate kapena kumwa madzi.*" [Eksodo 34:28]

"*Ndipo pamene ponse musala kudya musakhale ndi nkhope yachisoni ngati onyengawo; pakuti aipitsa nkhope zao kuti aonekere kwa anthu kuti alimkusala kudya. Inde ndinena kwa inu, iwo alandiriratu mphoto zao. Koma iwe, posala kudya dzola mutu wako, ndi kusamba nkhope yako; kuti usaonekere kwa anthu kuti ulikusala kudya, koma kwa Atate wako ali m'tseri: ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.*" [Mateyu

6:16-18]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kusala unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena satsatira michitidwewu?
- Nanga lero lino, kodi ndianthu atl omwe amalemekezabe ndi kutsatira mchitidwewn?

***

## MUTU 5

### Kuyeretsa ziwalo (mapemphero asanachitike) m'Baibulo

Chipangano Chakale, ngakhalenso Chatsopano, chimalongosola za kufunika koyeretsa thupi munthu asanachite mapemphero. Izi ndizomwe Yesu (MUPI), ngakhalenso atumiki a Mulungu omwe analipo Yesu (MUPI) asanabwere, ankachita. Munthu asanapemphere ayenera kuyeretsa ziwalo zina za thupi lake monga manja, nkhope, mapazi ndi zina zotero.

1. **Mose** ndi Aroni (MUPI) adziyeretsa potsuka manja ndi mapazi awo asanapemphere: "*Ndipo anaika mkhate pakati pa chihema chokomanako, ndi guwa la nsembe; nathiramo madzi osamba. Ndipo Mose ndi Aroni ndi ana ache amuna anasamba manja ao ndi mapazi ao m'menemo... monga Yehova adamuuza Mose.*" [Eksodo 40:30-31]

<u>Ndemanga</u>

Mose ndi Aroni (MUPI) sanasambitse manja ndi mapazi awo mwakufuna kwawo ayi. Iwo anachita izi chifukwa Mulungu <u>*adamuuza*</u> Mose kuti iwo azitero.

2. **Davidi** (MUPI) asamba asanapemphere: "*Pamenepo Davide ananyamuka pansi, nasamba, nadzola, nasintha zobvala; <u>nafika</u> ku <u>nyumba ya Yehova</u>, <u>napembedza</u>...*" [2 Samueli 12:20]

3. **Paulo** adziyeretsa asanalowe m'Kachisi "*Pamenepo Paulo anatenga anthuwo, ndipo m'mawa mwache m'mene <u>anadziyeretsa</u> nao pamodzi analowa m'Kachisi...*" [Machitidwe 21:26]

<u>Ndemanga</u>

Nayenso Paulo, yemwe ali wotsatira wa Yesu (MUPI), ankadziyeretsa asanapemphere. Apa ndizachionekere kuti Paulo sankadziyeretsa ndi cholinga china ayi, koma chokachita mapemphero. Yesu (MUPI) nayenso ankadziyeretsa asanapemphere. Iye ankachita izi potsatira mchitidwe wa atumiki a Mulungu omwe analipo iye asanabwere, ngati momwe akunenera m'Baibulo:

"*Musaganize kuti ndinadza ine kudzapasula chilamulo kapena (machitidwe) a aneneri; sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa*" [Mateyu 5:17]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kusambitsa ziwalo (thupi) mapemphero asanachitike unanka kuti?
- Nchifukwa chiyani lero lino anthu ena satsatira mchitidwewu?
- Nanga lero lino, ndianthu ati omwe amalemekezabe ndi kutsatira mchitidwewu?

***

## MUTU 6

## Mdulidwe m'Baibulo

Yesu (MUPI), ngakhalenso aneneri ndi atumiki a Mulungu omwe analipo iye asanabwere kuyambira pa Abrahamu (MUPI), analandira mdulidwe. Baibulo limati mchitidwewu uyenera kutsatiridwa mpaka kalekale.

"*Ndipo pamene panakwanira masiku asanu ndi atatu akumdula iye, anamutcha dzina lache Yesu, limene anatchula mngeloyo asanalandiridwe iye m'mimba.*" [Luka 2:21]

"*Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, koma iwe uzikumbukira pangano langa, iwe ndi mbeu zako za pambuyo pako m'mibadwo yawo.*" [Genesis 17:9]

<u>Ndemanga</u>

Izi zikuonetsa kuti mchitidwe wa mdulidwewu

unakhazikitsidwa kuti uzichitika mpaka muyaya.

"*Ili ndi pangano langa limene uzisunga pakati pa ine ndi iwe ndi mbeu zako za pambuyo pako: azidulidwa amuna onse a mwa inu.*" [Genesis 17:10]

<u>Ndemanga</u>

Malingana ndi ndimeyi, ana enieni ochokera mwa Abraham (MUPI) ndi omwe amalemekeza ndi kutsatira mchitidwe wa mdulidwewu.

"*Muzidula khungu lanu; ndipo chidzakhala chizindikiro cha pangano pakati pa Ine ndi inu.*" [Genesis 17:11]

Ndemanga

Maganizo a Paulo (omwe titawakambirane nthawi ina) pa za mdulidwe akutsutsana kwambiri ndi lamulo loti amuna azilandira mdulidwe.

"*(ana) A masiku asanu ndi atatu azidulidwa mwa inu...*" [Genesis 17:12]

Ndemanga

Zoti amuna azidulidwa si mawu okuluwika ayi. Mawuwa ndi omveka bwino ndipo akutanthauza zomwe akunena. Pofuna kukwaniritsa pangano lamuyaya la pakati pa Mulungu ndi Abrahamu (MUPI), Yesu (MUPI) analandira mdulidwewu ali ndi masiku asanu ndi atatu, ngati momwe malamulo m'Baibulo akunenera. Choncho, chizindikiro cha mdulidwe chikhoza kutidziwitsa otsatira enieni a Yesu komanso a Abrahamu (MUPI).

Funso

Nanga, kodi ndi ndani yemwe anathetsa lamulo la mdulidwe pakati pa Akhrisitu?

Yankho

Lero lino, Akhrisitu samalandira za mdulidwe chifukwa cha momwe Paulo anatanthauzira lamulo la mdulidwe m'Baibulo. Iye anatanthauzira lamuloli molakwika ponena kuti mdulidwe womwe umanenedwawu si mdulidwe wa khungu ayi, koma wa mtima, chikhalirecho Yesu (MUPI) mwini wake analandira mdulidwe wa khungu.

**Nawu umboni wochokera m'Baibulo wa zomwe Paulo akukamba pa za mdulidwe**:

M'kalata yake kwa Aroma, Paulo akuti:

"…*koma Myuda ndiye amene akhala wotere mumtima; ndipo mdulidwe uli wa mtima, mu mzimu, si m'malembo a...*" [Aroma 2:29]

M'kalata yake kwa Agalatia, Paulo akuti:

"*Taonani, ine Paulo ndinena ndi inu, kuti, ngati mulola akuduleni, Khrisitu simudzapindula naye kanthu.*" [Agalatiya 5:2]

<u>Ndemanga</u>

Yesu sanalandire mdulidwe wa mtima. Kuonjezera apo, iye sanayankhulepo za mdulidwe wa mtima. Yesu anasunga pangano lomwe lili la muyaya polandila mdulidwe wa khungu.

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa mdulidwe unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena satsatira mtchitidwewu?
- Nanga lero lino, kodi ndianthu ati omwe amalemekezabe ndi kutsatira mchitidwewu?

***

## MUTU 7

### Nkhumba, nyama yodetsedwa m'Baibulo

Nkhumba ndi nyama yodetsedwa m'Baibulo

"*...ndi nkhumba, popeza igawanika chiboda, koma yosabzikula, muiyese yodetsedwa. Nyama yache musamaidya, mitembo yake musamaikhudza; muziyese zodetsedwa.*" [Levitiko 11:7-8]

"*...ndi nkhumba, popeza igawanika ziboda koma yosabzikula, muiyese yodetsa; musamadya nyama yao, musamakhudza mitembo yao.*" [Deuteronomo 14:8]

Zikuoneka kuti Yesu (MUPI) sankadya nyama ya nkhumba chifukwa Baibulo limanena kuti iye anabwera kudzalemekeza ndi kudzatsatira malamulo a Mose (MUPI). Yesu (MUPI) akunena m'Baibulo kuti:

"*Musaganize kuti ndinadza Ine (Yesu) kudzapasula chilamulo kapena (machitidwe) a aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa.*" [Mateyu 5:17]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kusadya nyama ya nkhumba unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena amadyabe nyama ya nkhumba?
- Nanga lero lino, kodi ndianthu ati omwe sadya nyama ya nkhumba?

***

## MUTU 8

## Mowa, Chakumwa choletsedwa m'Baibulo

Mowa ndiwoletsedwa m'Chipangano Chakale komanso m'Chipangano Chatsopano.

Chipangano Chakale "*Naipo Yehova ananena ndi Mose, nati, Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao mwamuna kapena mkazi akadzipatulira kulonjeza chowinda cha Mnaziri, kudzipatulira kwa Yehova; azisala vinyo ndi kachasu; asamwe vinya wosasa, kapena kachasu wosasa...*" [Numeri 6:1-4]

"*Vinyo achita chiphwete, chakumwa chaukali chisokosa; wosochera nazo alibe nzeru.*" [Miyambo 20:1]

"*Kuli kwabwino kusadya nyanma, kapena kusamwa vinyo...*" [Aroma 14:21]

Chipangano Chatsopano "*Pakuti iye adzakhala wamkulu pamaso pa Ambuye, ndipo sadzamwa konse vinyo kapena kachasu...*" [Luka 1:15]

Ndemanga

Zipangano zonse ziwiri zikulongosola momveka bwino kuti mowa ndi woletsedwa. Ngakhale izi zili chonchi, mabuku ena m'Baibulo lomweli amaloleza kumwa mowa. Koma kuti munthu amvetse ndi kudziwa zoona zokhazokha, ayenera kuunika ndime zomwe zimaletsa komanso zomwe zimaloledza mchitidwe womwa mowa zomwe zili m'musizi:

Kodi mowa m'Baibulo, ndiwoletsedwa kapena wololedwa?

**Unikani ndi kusankha nokha!**

**Siyanitsani A ndi B**

| A | B |
|---|---|
| **Wololedwa** | Woletsedwa |
| **m'Chipangano Chatsopano** | **m'Chipangano Chatsopano** |
| I Timoteo 5:23 | Luka 1:15 |
| "Usakhalenso wakumwa madzi wokha, komatu uchite naye vinyo pang'ono, chifukwa cha mimba yako ndi zofooka zako..." | "Pakuti iye adzukhala wamkulu pamaso pa Ambuye, ndipo sadzamwa konse vinyo kapena kachasu..." |

<u>Ndemanga</u>

Sizotheka kuti mowa ungakhale wololedwa komanso woletsedwa nthawi imodzi! Apa tikhoza kunena motsindika kuti Baibulo limadzitsutsa lokha. N'zokhumudwitsa kuti kudzitsutsa kwa Baibuloku, kunadza chifukwa cha kusamvetsa bwino malemba a Baibulo kwa alembi, makamaka panthawi yomwe amatanthauzira Baibulo kuchokera ku Chigiriki n'kupita kuziyankhulo zina. Nazi zitsanzo zina zakutsutsana kwa ndime zina m'Chipangano Chakale komanso Chatsopano. Nthawi ino, mulinso ndi ufulu owunika ndime zotsutsana za m'Baibulo zomwe zikutsatirazi ndi kudzisankhira nokha mbali imodzi:

**Siyanitsani A ndi B**

**Zaka zisanu ndi zitatu kapena khumi mphambu zisanu ndi zitatu?**

## Chipangano Chakale

A

2 Mbiri 36:6

Yehoyakini anali wa zaka zisanu ndi zitatu polowa ufumu...

B

2 Mafumu 24:8

Yehoyakini anali wa zaka khumi mphambu zisanu ndi zitatu polowa iye ufumu wake

## Chipangano Chatsopano

**Ndi ndodo kapena opanda ndodo?**

**A**

**Mateyu 10:10**

(Musadzitengere)... thumba la kamba la kunjira, kapena malaya awiri, kapena nsapato, kapena ndodo

**B**

**Marko 6:8**

...ndipo anawauza kuti asatenge kanthu ka paulendo, koma ndodo yokha...

Ndime zina zotsutsana m'Baibulo ndi izi:

**2 Samueli 24:13 imatsutsana ndi 1 Mbiri 21:11-12 2**

Samueli 24:13

Chomwecho Gadi anafika kwa Davide, namuuza, nanena naye, kodi zikugwereni m'dziko mwanu zaka zisanu ndi ziwiri za njala? Kapena muthawe adani anu akukupitikitsani miyezi itatu?

1 Mbiri 21:11-12

Naza Gadi kwa Davide, nanena naye, Atero Yehova, Dzitengereko; kapena zaka zitatu za njala kapena miyezi itatu ya kuthedwa pamaso pa adani ako

**Numeri 4:3 imatsutsana ndi Numeri 8:24**

| Numeri 4:3 | Numeri 8:24 |
|---|---|
| Kuyambira zaka makumi atatu ndi mphambu, kufikira zaka makumi asanu, onse akulowa utumikiwu kuti agwire ntchito ya chihema chokomanako. | Kuyambira ali wa zaka makumi awiri ndi zisanu ndi mphambu azilowa kutumikira utumikiwu mu ntchito ya chihema chokomanako. |

**Marko 16:2 imatsutsana ndi Yohane 20:1**

| Marko 16:2 | Yohane 20:1 |
|---|---|
| Ndipo anadza kumanda mamawa tsiku loyamba la Sabata, litaturuka dzuwa | Koma tsiku loyamba la Sabata anadza Maria wa Magadala mamawa, kusanayambe kucha, kumanda, napenya mwala wochotsedwa kumanda. |

**Luka 23:26 imatsutsana ndi Yohane 19:16**

| Luka 23:26 | Yohane 19:16 |
|---|---|
| Ndipo popita naye, anagwira munthu, Simoni wa ku Kurene ali kuchokera ku munda, namsenza iye mtanda aunyamule pambuyo pa Yesu. | Ndipo pamenepo anampereka iye kwa iwo kuti ampachike |

<u>Ndemanga</u>

Ndipovuta munthu kudziwa ngati Yehoyakini anali ndi zaka zakubadwa zitatu kapena khumi mphambu zisanu ndi zitatu pamene ankayamba kulamulira. Kulephera kusiyanitsa pakati pa manambala awiriwa, 8 ndi 18, kwapangitsanso kuti imodzi mwa ndime zotsutsana ziwirizi ikhale ndi umboni wolakwika. Kusiyanitsa kwa kalembedwe ka liwu kukhozanso kubweretsa kusiyana kwa tanthauzo la liwulo. Mwachitsanzo,

kuonjezera **sa** ku mneni kukhozanso kubweretsa kusiyana m'matanthauzo m'Baibulo, ngati momwe zilili ndi nkhani ija ya mowa komanso nkhani ya ndodo.

Ndiye funso n'kumati: 'Kodi malembo awiri okha n'kubweretsa mavuto anji ku Baibulo? Ndipo ine ndikuti, akhoza kusintha tanthauzo la lamulo la Mulungu. Mwachitsanzo, lamulo lakuti 'Usabe' likhoza kukhala 'Ube'.

Tsopano tikhoza kunena mosapeneka kuti mowa, womwe umaledzeretsa, suyenera kumwedwa. N'zokhumudwitsa kuti malemba a Chikhrisitu anasinthidwa kotero kuti m'Baibulo muli mawu ambiri otsutsana. Kodi ndindani yemwe angaleke kumwa mowa ngati malemba akunena kuti Yesu anasintha madzi kukhala vinyo ndicholinga choti omutsatira ake amwe ndi kusangalala?

**Kuloledwa kwa Mowa**

**Mafunso ambiri; mayankho ochepa!**

Nthano yosintha madzi kukhala mowa imapezeka mu Uthenga Wabwino wa Yohane wokha, womwe nthawi zambiri umatsutsana ndi Uthenga Wabwino wina (wa Mateyu, Mariko ndi Luka). Poyamba Mpingo unkadana ndi Uthenga Wabwino wa Yohane, kotero kuti unautcha uthengawu kuti ndi 'wa m'maluwa. Ndipo chifukwa choti Uthenga Wabwino winawo umafotokoza mofanana momwe moyo wa Yesu unalili, anautcha kuti ndiuthenga 'weniweni'

*[The New Encyclopaedia Britannica Vol 5 pg 379]*

- Ngati zili zoona kuti Yesu (MUPI) anasinthadi madzi kukhala vinyo, nanga ndichifukwa chiyani Luka (Luka 1:15) ndi Paulo (Aroma 14:21), omwe amatchedwa otsatira a Yesu (MUPI) analetsa kumwa mowa?
- Uthenga Wabwino wa Yohane sungakhale wolondola ndi

wopambana kwambiri kuposa mabuku a Luka ndi Aroma chifukwa uthengawu, malingana ndianthu ophunzira bwino za Chikhrisitu, unalembedwa mochedwa, mu chaka cha 85 A.D, pamene bukhu la Luka linalembedwa mu 70 A.D, ndipo bukhu la Aroma linalembedwa mu 56 A.D. Mabuku a Luka ndi Aroma analembedwa moyambirira patatsala zaka za pakati pa 20 ndi 30 kuti bukhu la Yohane lilembedwe.

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kusamwa mowa unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena amamwabe mowa?
- Nanga lero lino, ndianthu ati omwe amatsatirabe lamulo la kuletsa mowa?

***

## MUTU 9

## Kuvala mpango m'mutu kwa azimayi podzilemekeza m Baibulo

Azimayi onse omwe ankakhala pafupi ndi Yesu (MUPI) amabisa tsitsi lawo mu mpango. Uwu unalinso mchitidwe wa azimayi omwe ankakhala limodzi ndi atumiki oyambirira. Azimayi ankavala zovala zosathina ndi zobisa thupi lonse, kuphatikizapo tsitsi, ndipo nthawi zina, nkhope. Iwo ankachita izi podzisungira ulemu komanso powachitira manyazi anthu achilendo.

"*Ndipo Rebeka anatukula maso ache, ndipo pamene anaona Isake anatsika pa ngamila. Ndipo anati kwa mnyamata, 'Munthuyo ndani amene ayenda m'munda kukomana ndi ife?' Mnyamatayo ndipo anati, Uyo ndi mbuyanga: chifukwa chake namwali anatenga chophimba chake nadziphimba.*" [Genesis 24:64-65]

Ndemanga

Rabeka anafunditsa mutu wake pamaso pa mwamuna osamudziwa chifukwa chamanyazi ndi chofuna kudzisungira ulemu wake. Ngakhale lero lino, azimayi ofuna kudzisungira okha ulemu amachitabe ngati momwe Baibulo likunenera.

"*Koma mkazi yense wakupemphera, kapena kunenera, wobvula mutu, anyoza mutu wake; pakuti kuli chimodzimodzi kumetedwa.*" [1 Akorinto 11:5]

"*Pakuti ngati mkazi safunda, asengedwenso; koma ngati kusengedwa kapena kumetedwa kuchititsa manyazi apfunde.*" [1 Akorinto 11:6]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa azimayi wobitsa thupi lawo podzisungira ulemu unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino azimayi samalemekeza ndi kutsatira mchitidwewu?
- Nanga lero lino, kodi ndi azimayi ati omwe amatsatirabe mchitidwewu?

***

# MUTU 10

## Kulonjerana pofunirana mtendere m'Baibulo

Yesu (MUPI), kuphatikizirapo anthu omwe ankakhala naye pafupi amalonjerana pofunirana mtendere m'moyo wawo.

"...*Yesu anadza naimirira pakati pao, nanena nawo, Mtendere ukhale ndi inu*." [Yohane 20:19]

"*Davide natuma anyamata khumi, nanena kwa anyamatawo: mumuke kwa Nabala ndi kundilankhulira iye; ndipo muzitero kwa wodalayo, Mtendere ukhale pa inu*…" [1 Samueli 25:5-6]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kulonjerana pofunirana mtendere unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena samalemekeza mchitidwewu?
- Nanga lero lino, ndianthu ati omwe amasatirabe mchitidwewu?

***

# MUTU 11

## Katapira, mchitidwe woletsedwa m'Baibulo

Katapira ndi ndalama zoonjezera zomwe munthu amapereka pobweza ngongole. Malingana ndi Chipangano Chakale, mchitidwe wa katapira ndi wosavomerezeka.

"*Musamakongoletsa m'bale wanu mopindulitsa; phindu la ndalama, phindu la chakudya, phindu la kanthu kali konse kokongoletsa.*" [Deuteronomo 23:19]

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kusachita katapira unanka kuti?
- Kodi n'chifukwa chiyani lero lino anthu ena amachitabe katapira?
- Nanga lero lino, ndianthu ati omwe sachita mchitidwewu?

***

## MUTU 12

### Mitala, mchitidwe wovomerezeka m'Baibulo

Mwamuna amakhala pa mitala akakhala pa banja ndi akazi osachepera mmodzi. Atumiki ambiri ankachitanso mitala.

"*Ndipo Sarai mkazi wache wa Abramu anatenga Hagara mdzakazi wache wa ku Aigupto, Abramu atakhala m'dziko la Kanani zaka khumi, nampereka iye kwa Abramu mwamuna wache, kuti akhale mkazi wache…*" [Genesis 16:3]

"*Ndipo Davide anakhala ndi Akisi ku Gati, iye ndi anthu ache, munthu yense ndi a pabanja pache, inde Davide ndi akazi ache awiri.*

[1 Samueli 27:3]

Ndime zina za m'Baibulo zomwe zikuchitira umboni pa nkhani ya mitalayi ndi izi:

"*Ndipo anali nao akazi mazana asanu ndi awiri...*" [1 Mafumu 11:3]

"*Ndipo Rehabiamu anakonda Maaka mwana wamkazi wa Abisalomu kuposa akazi ache onse, ndi akazi ache ang'ono (pakuti adatenga akazi khumi asanu ndi atatu, ndi akazi ang'ono makumi asanu ndi limodzi...*" [2 Mbiri 11:21]

"*Munthu akakhala nao akazi awiri, wina wokondana naye wina wodana naye, nakam'balira ana, wokondana naye, ndi wodana naye yemwe; ndipo mwana wamwamuna woyamba akakhala wa iye uja anadana naye; pamenepo kudzali, tsiku lakugawira ana ache amuna chuma chake, sangakhoze kuyesa mwana wa wokondana naye woyamba kubadwa, Wosati mwana wa wodana naye, ndiye woyamba kubadwatu*" [Deuteronomo 21:15-16]

“...*Usamtenga mkazi kumuonjezera kwa mbale wache*...” [Levitiko 18:18]

Ndemanga

Palibe umboni wina uliwonse womwe umanena kuti Yesu (MUPI) analetsa kuchita mitala. Yesu (MUPI) akanaletsa mchitidwe wa mitala, akadaonetsa ngati akudana ndi zomwe ankachita atumiki omwe analipo iye asanabwere.

**Ophunzira bwino za Baibulo avomereza mitala**

Bambo Eugene Hillman, m’bukhu lake lotchedwa, ‘Polygamy Reconsidered akulongosola kuti:

“*Palibe ngakhale ndime imodzi mu Chipangano Chatsopano momwe muli lamulo lonena kuti mwamuna azikwatira mkazi mmodzi yekha basi.*” [Polygamy Reconsidered]

Iye ponena akuti Mpingo (wa Chikhrisitu) ku Rome unathetsa mchitidwe wa mitala ndicholinga chofuna kuti anthu asamachite zosemphana ndi chikhalidwe cha ku Greece ndi Rome chomwe chimalola mwamuna kukwatira mkazi mmodzi yekha basi ngakhale chikhalidwechi sichimaletsa mchitidwe wonyansa wachiwerewere.

Tsopano, munthu aliyense ayenera kulingalira izi:

- Kodi mchitidwe wa kuchita mitala unanka kuti?
- Kodi n’chifukwa chiyani lero lino anthu ena sachita mitala?
- Nanga lero lino, kodi ndianthu ati omwe amalemekezabe ndi kutsatira mchitidwewu?

Tsopano, tiyenera tifufuze anthu omwe lero lino amalemekeza ndi kutsatira chiphunzitso cha Baibulo. Chipembedzo chomwe chimalemekeza ndi kutsatira chiphunzitso cha Baibulo ndi

## CHISILAMU!

Asilamu amanena kuti iwo amatsatira chiphunzitso cha Mtumiki Yesu (MUPI) komanso ziphunzitso za atumiki ena a Mulungu omwe analipo Yesu (MUPI) asanabwere. Tsopano, tiyeni tione ngatidi izi zili zoona. Takambirana kale za machitidwe a Yesu (MUPI), ndipo tsopano tiyenera kusiyanitsa machitidwewa ndi machitidwe a Asilamu.

Bukhu la *Qur'an* likugwirizana kwatunthu ndi ziphunzitso za m'Baibulo zomwe takambirana kale zija motere:

**1. Umodzi wa Mulungu m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*…palibe wina wompembedza mwachoonadi, koma Ine; choncho ndilambireni.*" [Qur'an 21:25]

**2. Kugwetsa nkhope pansi popemphera m'**Qur'an

Mulungu akuti: "*Uwaona akugwira m'maondo ndi kugwetsa nkhope zawo pansi ncholinga chofuna zabwino za Mulungu ndi chikondi (chake). Zizindikiro zawo zili pankhope zawo zosonyeza kulambira kwawo*. [Qur'an 481:291

**3. Lamulo lopereka chaulere kwa anthu osowa m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Akufunsa kuti apereke chiyani? Nena: Chuma chilichonse chimene mungachipereke, (chiperekeni) kwa makolo awiri, achibale, kwa ana amasiye, kwa osauka, ndi kwa apaulendo. Ndipo chabwino chilichose chimene mungachite, ndithudi, Allah akuchidziwa.*" [Qur'an 2:215]

**4. Kusala m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ee inu amene mwakhulupilira! Kwalamulidwa*

*kwa inu kusala (Ramadhan) monga momwe kudalamulidwira kwa anthu akale inu musadabwere kuti muope Allah (popewa zoletsedwa).*" [Qur'an 2:183]

Asilamu alamulidwa kusala kwa masiku makumi ndi atatu (30) m'mwezi wolemekezeka wa Ramadhan. M'mweziwu, iwo samadya, samamwa, kapena kugonana kuchokera m'bandakucha kufikira kulowa kwa dzuwa.

**5. Kuyeretsa ziwalo (mapemphero asanachitike) m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ee inu amene mwakhulupilira! Pamene mwaimilira kuti mukaswali, sambitsani nkhope zanu, ndi manja anu mpaka mmagongono; ndipo pakani madzi pamitu panu ndi kusambitsa mapazi anu mpaka mu akakolo.*" [Qur'an 5:6]

**6. Mdulidwe m'Hadeeth**

Mtumiki Muhammad (MUPI) akunena kuti:

"Pali zinthu zitatu zomwe ndimachitidwe a atumiki: kulandila mdulidwe, kumeta mavuzi ndi bweya la ku nkhwapa, kuwenga zala ndi kupungula tsitsi la pamulomo wa pamwamba. [Al-Bukhari]

Msilamu aliyense wachimuna mpaka lero lino amalandirabe mdulidwe. Iye ayenera kudulidwa pakatha masiku asanu ndi atatu chibadwire, ngati momwe analamulira Muhammad (MUPI), yemwe tonse tikudziwa kuti anabwera pambuyo pa Yesu (MUPI).

**7. Nkhumba, nyama yoletsedwa m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Kwaletsedwa kwa inu (kudya) chakufa chokha, ndi liwende ndi nyama yankhumba, ndi chomwe chazingidwa m'dzina osati la Allah...*" [Qur'an 5:3]

**8. Mowa, chakumwa choletsedwa m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ee, inu amene mwakhulupilira! Ndithudi, mowa (kutchova) njuga, kupembedza mafano ndi kuombeza maula (zonsezi) ndi uve, mwa ntchito za Satana. Choncho, zipeweni kuti mupambane.*" [Qur'an 5:90]

**9. Kuvala mpango m'mutu kwa azimayi podzilemekeza m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ndipo auze Asilamu achikazi kuti adzolitse maso awo ndikusunga umaliseche wawo. Ndipo asaonetse (poyera zomwe amadzikongoletsa nazo kupatula zimene zaonekera poyera (popanda cholinga chotero). Ndipo afunde kumutu mipango yawo mpaka m'zifuwa zawo...*" [Qur'an 24:31]

Chifukwa chomwe Mulungu walamulira azimayi kuti azibisa matupi awo chomwenso chikupezeka m'Quran ndi choti mchitidwewu umasiyanitsa azimayi osakhulupilira ndi okhulupilira, omwe amadzipatsa ulemu povala zovala zosathina ndi zazitali. Mchitidwewu umawateteza azimayi okhulupilirawa ku mnyozo wa anthu.

**10. Kulonjerana pofunirana mtendere m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ee, inu amene mwakhulupilira! Musalowe m'nyumba zomwe sinyumba zanu kufikira mutapempha chilolezo poodira ndikupereka salaamu kwa eni nyambazo.*" [Qur'an 24:27]

Asilamu amalonjerana pofunirana mtendere wina ndi mzake. Pamene iwo akumana, mmodzi amanena mawu a m'chiArabu oti: 'As-Salaam alaikum' kutanthauza kuti 'Mtendere ukhale ndi inu'. Ndipo nzakeyo ali okakamizidwa kuyankha kuti: 'Wa-alay-kumus-salaam (Mtendere ukhalenso ndi inu nomwe)'. Izi ndi zomwenso Yesu (MUPI) ankachita.

**11. Katapira, mchitidwe woletsedwa m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ee! Inu amene mwakhulipilira! Opani Allah, ndipo siyani zimene zatsalira m'katapira, ngati inu mulidi okhulupilira.*" [Qur'an 2:278]

**12. Mitala, mchitidwe wovomerezeka m'Qur'an**

Mulungu akuti: "*Ngati mwaopa kuti simungachite chilungamo pa amasiye (opaninso kusawachitira chilungamo akazi pamitala), choncho kwatirani amene mukuwafuna mwa akazi; awiri, kapena atatu, kapena anayi (basi). Koma ngati mukuopa kuti simungathe kuchita chilungamo, (kwatirani) mmodzi basi...*" [Qur'an 4:3]

***

Asilam amanena kuti iwo amalemekeza ndi kutsatira machitidwe a Yesu (MUPI), ngati momwe kabukhuka kakulongosolera. Kodi kwa iwowa, Yesu (MUPI) ndi ndani?

Yesu (MUPI) ndi mmodzi wa atumiki odziwika bwino a Mulungu. Iye anabadwa mozizwitsa popanda bambo. Iye simwana wa Mulungu ndipe iye simmodzi wa 'utatu wa Mulungu'. Ngakhale iye mwini ananena kuti iye anali mtumiki wa Mulungu, osati mwana Wake. Iye sanafere machimo a munthu wina aliyense. Iye sanapachikidwe pamtanda, kuphedwa kapena kuukitsidwa kwa akufa, koma anatengedwa ndi Mulungu kupita kumwamba.

**Kodi Yesu ankapembedza bwanji?**

Momwe Yesu (MUPI) ankapembedzera Mulungu zanenedwa kale. Yesu (MUPI) ankapembedza Mulungu ngati momwe Asilamu amachitira. Choncho, tikhoza kunena kuti Asilamu amapembedza mofanana ndi momwe anthu amachitira nthawi ya Yesu (MUPI). Ichi ndi chifukwa chake Asilamu amanena kuti iwo, osati Akhrisitu alero lino, ndi omwe amatsatira mwachoonadi chipembedzo cha Yesu (MUPI). Tikhoza kunenanso kuti omwe ankatsatira Yesu (MUPI) mwachoonadi pachiyambi ndi Asilamu alero. Akhrisitu alero amamutsatira Yesu (MUPI) mu dzina lokha osati m'chipembedzo ngati momwe Asilamu amachitira.

**Asilamu amanena kuti iwo ndi otsatira enieni a Yesu (MUPI). Nanga chinachitika n'chiyani kuti Chikhrisitu chikhale chosochera?**

Yesu (MUPI) atachoka padziko lapansi, panali anthu ena odalitsika omwe ankatsatira chiphunzitso chenicheni cha Yesu (MUPI). Ndipo Muhammad (MUPI) atabwera, anthuwa anaudzindikira uthenga wake ndipo anaulandira ndimanja awiri. Zofanana zomwe Yesu (MUPI) ndi Muhammad (MUPI) analinazo zinawapangitsa anthu kuika chikhulupiliro chawo pa Muhammad (MUPI). Iwo ankamukhulupilira Muhammad (MUPI) kaamba koti kubwera kwake kunalembedwa mu Uthenga Wabwino wa Yesu (MUPI). Kubwera kwa Muhammad (MUP), chimodzimodzinso kwa Yesu (MUPI), kunaloseredwa ndi Mose (MUPI).

Nthawi ya Muhammad (MUPI), anthu onse omwe sankakhulupilira mwa iye ankachita zosemphana ndi chiphunzitso chenicheni cha Yesu (MUPI). Izi zinagawanitsa mpingo, ndi kupangitsa kuti pakhale mitundu yosiyanasiyana ya ma Baibulo padziko. Kusiyana kwa mipingo ndi ma Baibulo ndiumbori wokwanira kwa Akhrisitu woti chipembedzo chawo chimachita zotsemphna ndi chiphunzitso chake choyambilira. Ichi ndichifukwa chake Asilamu amanena kuti uthenga womwe atumiki onse ankalalikira umapezeka m'Chisilamu.

**Asilamu amati iwo ndi otsatira enieni a Yesu (MUPI). N'chifukwa chiyani iwo samatchedwa Akhrisitu?**

M'Baibulo, mulibe malo ngakhale amodzi omwe akunena kuti Yesu (MUPI) anazitcha yekha kuti iye ndi Mkhrisitu. Malingana ndi Baibulo, liwu loti 'Mkhrisitu' linatchulidwa poitanira Akhrisitu mu chaka cha 43 A.D. basi, ndipo panthawiyi n'kuti Yesu (MUPI) anali atatengedwa kale ndi Mulungu kupita kumwamba.

Liwu limeneli linayamba kugwiritsidwa ntchito ndi Ayuda osakhulupilira ku Antiyokeya mu chaka cha 43 A.D. Bukhu la Machitidwe m'Baibulo likuchitirapo umboni pankhaniyi motere:

"…*ndipo ophunzira anayamba kuchedwa Akhrisitu ku Antiokeya*." [Machitidwe 11:26]

Dzinali latchulidwa kachiwiri pa Machitidwe 26:28, ndipo latchulidwa kachitatu pa I Petro 4:16. Tikaphatikizira, dzinali latchulidwa katatu kokha mu Chipangano Chatsopano. Ngakhale izi zili chomwechi, dzinali silinatchulidwepo m'moyo wonse wa Yesu (MUPI) padziko lapansi.

**Kodi pali ubale wanji pakati pa Yesu, Mose ndi Muhammad (MUPI)**

Yesu (MUPI) ankalalikira uthenga womwe Mose (MUPI) ankalalikira. Chipangano Chakale chinalosera za kubwera kwake, ndipo otsatira a Mose (MUPI) amayenera kumutsatira iye. Yesu (MUPI) nayenso analosera za kubwera kwa mtumiki wina wotchedwa Muhammad (MUPI) yemwe adzabwere pambuyo pake. Otsatira mtumiki aliyense amayenera kutsatira atumiki omwe analonjezedwa m'mabuku awo opatulika chifukwa choti mtumiki wina aliyense amanena kuti anabwera kudzakwaniritsa, osati kudzathetsa, malamulo a mtumiki yemwe analipo iye asanabwere (Mateyu 5:17-18]

**Kodi Asilamu amakhulupilira Uthenga Wabwino wa Yesu?**

Inde. Asilamu onse amakhulupilira uthenga omwe unavumbulutsidwa kwa Yesu (MUPI), ndipo ngati iwo satero, ndiye kuti sakhala Asilamu. Uthenga Wabwino wa Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane ndi Injeel, Uthenga Wabwino weniweni wa Yesu (MUPI). Ngakhale izi zili chonchi, Asilamu amakhulupilira mawu okhawo omwe Qur'an imavomelezana nawo. Asilamu amakhulupiliranso Torah (Bukhu lenileni la Chipangano Chakale lomwe linavumbulutsidwa kwa Mose (MUPI).

**Kodi Chisilamu chimatanthauza chiyani?**

Chisilamu chimatanthauza 'kugonjera' mwa Mulungu mmodzi

basi, yemwe ali Mlengi wa zonse. 'Chisilamu' ndi liwu la chiyankhulo cha chiArabu (Chiluya) ndipo limatanthauza 'mtendere. Mwachidule Msilamu ndi munthu yemwe amakhazikitsa mtendere pogonjera ku chifuniro cha Mulungu mmodzi.

**Kodi Asilamu amapembedza Muhammad (MUPI?**

Ayi. Asilamu amapembedza Mulungu **mmodzi yekha**, yemwe ali Mlengi wa zonse. Kwa iwo, Muhammad (MUPI) ndi mtumiki wa Mulungu yemwe ankalalikira uthenga woti Mulungu ndi mmodzi yekha. Iyenso mwini wake ankapembedza Mulungu **mmodzi** yemweyu.

**Kodi Muhammad (MUPI) anabwera ndi chipembedzo chatsopano?**

Muhammad (MUPI), chimodzimodzinso Yesu (MUPI), sanabwere kudzafalitsa chipembedzo chatsopano. Iye anabwera kudzaongola ndi kudzakwaniritsa uthenga wa Yesu (MUPI) womwe panthawiyi unali utasokonezedwa ndianthu omwe analipo Yesu (MUPI) atachoka. Ichi ndi chifukwa chomwe kuli koyenera kuti anthu azitsatira uthenga wa Chisilamu womwe Muhammad (MUPI) ankalalikira chifukwa sungawatengere iwo kuchionongeko. Iwo ayenera kutero ngati akufunadi kukhala okondeka pamaso pa Mulungu komanso Yesu.

**Kodi 'Allah' ndi ndani?**

**Allah** ndi dzina la Mulungu **mmodzi yekha**.

**Kodi Chikhulupiliro chomwe chamanga maziko a Chisilamu ndi chiti?** Maziko a Chisilamu agona pa kukhulupilira kuti Mulungu ndi mmodzi yekhayo yemwe ali woyenera kupembedzedwa.

**Kodi Qur'an ndi Chiyani?**

Qur'an ndi mawu enieni a Mulungu omwe anavumbulutsidwa

kwa Muhammad (MUPI). Ili ndi Bukhu lokhalo la Mulungu lomwe, kwa zaka zopitilira 1400 tsopano, silinasinthidwepo poonjezera kapena pochotsa liwu ngakhale limodzi lokha. Bukhuli likadali m'chiyankhulo chomwe linavumbulutsidwira, cha chiArabu.

**Malingana ndi Chisilamu, kuti munthu akapulumutsidwe ayenera kuchita chiyani?**

Choyamba, iye ayenera kukhulupilira kuti palibe mulungu wina woyenera kupembedzedwa, koma Mulungu Mmodzi yekha, ndiponso ayenera kukhulupilira kuti Muhammad (MUPI) ndi Mtumiki womaliza wa Mulungu.

Kenako, iye ayenera kugwira ntchito zabwino modzipereka kwa Mulungu ndicholinga chomusangalatsa Iye. Ntchito zabwino zomwe munthu angagwire ndi monga kupereka chaulere kwa osowa, kusala, kupemphera, kusamala anthu amasiye, ndi ntchito zina zotero. Ngati tichimwa m'moyo mwathu n'kulephera kugwira ntchito zotamandika pamaso pa Mulungu, tiyenera kulapa kwa Mulungu kuti atikhululukire machimo athu. Munthu ayenera kuvomereza kulakwa kwake asanalape, ndipo kulapa kwakeko kuyenera kukhala kochokeradi pansi pamtima wake.

***

## Mawu omaliza

Mukamaliza kuwerenga bukhuli, muona kuti ndi Chisilamu chokha chomwe chimalemekeza machitidwe a Yesu (MUPI). Mukhalsno mutadziwa kuti Chisilamu si chipembedzo chatsopano. Ichi ndi chipembedzo chomwe chimaika chikhulupiliro mwa Mulungu Mmodzi yekha. Ichinso ndi chipembedzo cha Yesu (MUPI) kuphatikizirapo atumiki ena omwe analipo iye asanabwere.

Kukhala Msilamu sikutanthauza kupanga chisankho pakati pa Muhammad (MUPI) kapena Yesu (MUPI). Kukhala Msilamu kumatanthauza kutsatira Yesu (MUPI) pochita zomwe ankaphunzitsa Muhammad (MUPI), yemwe anabwera kudzakwaniritsa uthenga wa Yesu (MUPI).

Ndikupempha Mulungu kuti awakhulululukire awerengi athu machimo awo, komanso akapangitse bukhuli kukhala njira yomwe ingawatengere anthu ku chipulumutso powaunikira chilungamo. Ndikupempha munthu wina aliyense kuti aziwerenga bukhu lolemekezeka la Qur'an Chifukwa:

- ndi mawu enieni a Mulungu omwe Iye ankawavumbulutsa pangonopang'ono momwe Iye ankafunira.
- silimadzitsutsa
- limapereka mayankho ku mavuto omwe anthu amakumana nawo pamoyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Limalongosolanso za moyo womwe uli mkudza
- ndi bukhu lokhalo lomwe linayamba kutetezedwa ndi kusungidwa pa mtima ndi anthu miyanda miyanda dziko lonse

lapansi kuchokera pamene linavumbulutsidwa kufikira lero lino.

- lili mu chiyankhulo chomwe linavumbulutsidwa, cha chiArabu.
- matanthauzo ake alibe zolakwika, zoonjezera, zochotsera kapena zolakwika zina zilizonse.
- silimatsutsana ndi Sayansi.
- silinasinthidwepo, ndipo limatetezedwa ndi kusungidwa bwino mu chiyankhulo chake chomwe linavumbulutsidwa.
- limaitanira wina aliyense ku chipembedzo chimodzi chomwe chimapezeka mibado yonse ya anthu.

***